


Baibulo ya ana
Ikupasilani

Chiyambi
chakukwiya kwa
munthus



Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Byron Unger; Lazarus
Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: M. Maillot; Tammy S.

Yotathauzidwa ndi: Phiri Williams

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2020 Bible for Children, Inc.


Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa
makopewa koma osagulitsa.



MULUNGU ANAPANGA ZONSE!

Pamene Mulungu analenga munthu
woyamba, Adamu, anakhala m'munda
wa yedeni ndi mkazi wake Eva.
Anakhala wosangalala komanso

womvera Mulungu ndi
wosangalala ndi kupezekwa
pamaso pa
Mulungu mpaka
tsiku limodzi ...





"Kodi Mulungu
anakuuzani kuti
musadye mtengo
uliwonse?" njoka

inafunsa Eva. "Tingathe kudya zipatso zonse
koma zamtengowu ayi," Eva anayankha. "Ngati
tizadya kapena kugwira zipatso zake, ifeyo
tizafa." "Ayi simuzafa."

Njoka inanena. "Inuyo
muzakhala ngati Mulungu."
Ndipo Eva anafuna chipatso
chamtengowo. Anamvera
njokayo

ndipo anadya chipatsocho.



Ndipo pamene Eva anachita
kusamvera kwa Mulungu
anamtsogolera Adamu kuti
adye chipatso. Ndipo
Adamu anakanena kuti,
"ayi! Sindikufuna
kusamvera mau
a Mulungu."





Pamene

Adamu ndi Eva atachimwa,
ndipo wonse anazindikira kuti
alimaliseche. Iwo anazipangira masamba
amkuyu. Anadziveka wokha, ndi kukabisala
kuthengo kuchoka pamaso pa Mulungu.




Kumadzulo Mulungu anabwera kuzayendera kumunda.
Iye anadziwa chimene Adamu ndi Eva anachita.
Ndipo Adamu anamuda mkazi wake Eva.
Ndipo Eva anayida njoka. Mulungu anati,
“njoka ndiyotembereredwa. Mkazi
azakhala ndi ululu poberekana.”

“Adamu, chifukwa wachimwa,
nthaka ndiyothemberererekana
ndi minga. Muzakhala
wobvutika pofuna
kupeza chakudya

chokoma
chatsiku
ndi tsiku.”





Ndipo Mulungu
anawachotsa Adamu
ndi Eva m'munda muja.
Chifukwa anachimwa,
azichotsa pakati
pa iye amene
amapeleka
moyo.





Mulungu anapanga lupanga wamoto
lowachotseramo m'munda. Mulungu
anawapangira zikopa za nyama
kwa Adamu ndi Eva.

Kodi Mulungu
zikopazi
anazitenga
kuti?




Nthawi imene banja limayamba kwa Adamu ndi Eva. Mwana wao woyamba, anali Kayini, wolima zam'munda. Mwana wao wachiwiri anali Abele woweta zoweta.




Tsiku lina Kayini anabweretsa masamba ngati mpatso kwa Mulungu. Ndipo Abele anabweletsa nkhosa zomwe zinali zapamtima pake ngatiso mpatso kwa Mulungu. Mulungu anakondwela ndi mphatso ya Abele.



Mulungu sanakondwere ndi mphatso ya Kayini. Ndipo Kayini anapsa mtima kwambiri. Koma Mulungu anati, "ngati muchita izo zomwe zolondola, kodi siungalandiridwe?"



Mkwiyo wa Kayini unakhala uli
mumtima wake. Mkupita kwa
nthawi kumunda kuja anamlonda
Abele - ndikumupha!



Ndipo Mulungu analankhula ndi Kayini. "Kodi mbale wako alikuti, Abel?" "ine sindikudziwa," Kayini nanama bodza. "Kodi ine ndine wosunga mbale wanga?" Mulungu anamlanga Kayini pomulanda katundu wake yense wakumunda ndi kumupanga iye kukhala woyenda yenda kusowa pokhala.



Ndipo Kaiyini anachoka pamaso pa Mulungu.
Anakwatira mwana wamkazi wa Adamu ndi Eva.
Ndipo banja lawo linakula. Zizukulu za
Kayini ndi zizukulu zazikulu za Kayini
zinazaza mzinda umene anaupeza iye.



Komabe, banja la Adamu ndi Eva
linakula mofulumira, ndipo m'matsiku
amenewo anthu anakhala padziko
kwa nthawi yayitali.



Pamene mwana wawo Seti anabadwa, Eva anati,
"Mulungu anandipasa Seti kuti alove mmalo
mwa Abele." Ndipo Seti anali wowopa
Mulungu nakhala zaka 912 ndikubeleka
ana ambiri.



Ndipo anthu pa dziko anakhala wochimwa kwambiri pamene mibadyo imachulukira churukila. Pomaliza penipeni, Mulungu anapanga chisankho choononga munthu ndi zilombo zonse ndimalame. Mulungu anakhala odandaula chifukwa chopanga



munthu.
Komabe
munthu mmodzi yekha
anamkondweretsa
Mulungu ...





Munthu ameneyu ndiye Nowa. Chidzukulu cha
Seti, Nowa anali woyela komanso wachilungamo.

Anayenda ndi Mulungu. Iye anaphunzitsa
ana ake atatu zakuwopa Mulungu.
Kenaka Mulungu anapanga njira
yomugwiritsa nchito
Nowa mwachilendo
ndi

modabwitsa!



Chiyambi chakukwiya kwa munthu

Nthano yochokera mu mau a Mulungu,
Baibulo,

opezeka mu

Genesis 3-6

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130





Mapeto



Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu
yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo.
Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri
ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi
kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na
pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni
akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera
kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu:
Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo
munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi
moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo
anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale
ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu
ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16

